# PHUMZIRO LA 40

1- Pamene Sawulo sanamumvere Mulungu, kodi Mulungu anamusankha ndani kuti akhale mfumu ya a Isirayeli yotsatira?
-Davide.

2- Kodi Sawulo ndi Davide anali osiyana bwanji?

-Sawulo sankakhulupilira kuti iye anabadwira mu tchimo ndipo ali osiyana ndi Mulungu, koma Davide amkakhulupilira.
-Sawulo sankakhulupilira kuti Mulugu amapereka chilango cha imfa pa tchimo lina lililonse, koma Davide ankakhulupilira.
-Sawulo sankakhulupilira kuti Mulungu yekha ndi amene anakatha kumupulumutsa iye, koma Davide ankakhulupilira.
-Sawulo sankakhulupilira mu chipangano cha Mulungu chakuti adzatumiza Mpulumutsi, koma Davide ankakhulupilira.

3- Kodi Davide atatha kumanga nyumba yache, ankafuna kupanga chiyani?
-Davide ankafuna kuti amange nyumba ya Ambuye.

4- Kodi amene adzamange nyumba ya Mulunguyo adzakhala ndani?
-Mwana wa mamuna wa Davide.

5- Kodi lonjezo lalikuru limene Mulungu anapereka kwa Davide linali lotani?
-Mulungu analonjeza zakuti adzatumiza Mpulumutsi kupitira mu zidzukulu za Davide.

6-Kodi Nyumba ya Mulungu imene Solomoni anamanga

imkafanana bwanji ndi Sakasa la Mulungu limene a Isila-
yeli anamanga mchipululu muja?
-Sakasa la Mulungu ndi Nyumba ya Mulungu, zonse zinali ndi chipinda choyamba chimene chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulika.
-Sakasa la Mulungu ndi Nyumba ya Mulungu, zonse zinali ndi chipinda chachiŵiri chimene chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulikitsitsa.
-Sakasa la Mulungu ndi Nyumba ya Mulungu, zonse zinali ndi nsaru yotchinga pakati pa zipinda ziŵiri zija.

7-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera ndipo amadana ndi tchimo lina lililonse, kodi wamsembe wamkulu amaloredwa kuloŵa M'chipinda Chopatulikitsitsacho kangati?
-kamodzi pa chaka.

8-Kodi wamkulu wamsembe ankachita chiyani Mchipinda Chopatulikitsitsachija?
-Ankamwaza magazi a nyama pamwamba pa Likasa la Chipangano lija.

9- Kodi Mulungu ankayenera kuti achite chiyani akaŵawona magazi a nyama amene wamkulu wamsembe amawawaza pa Likasa la Chilanga lija?
-Mulungu ankanena kuti adikira kaye osapereka msanga chilango cha machimo kwa chaka china chimodzi mpaka malipiro abwino a machimowo atachitika.

10- Kodi magazi a nyama ankatha kulipira pa sambi za a Isirayeli?
-Iyayi.

11- Kodi chifukwa chiyani magazi a nyama sanakatha kulipira pa sambi za anthu?
-Chifukwa chakuti sambi ziyenera kulipiridwa ndi imfa ya munthu wochimwa.



ngati iwowo sakutsata njira ya Mulungu, Mulungu adzaŵatumiza a Siliya kudzaŵagonjetsa iwowo pa nkhondo, ndikuŵachita ngati akapolo awo.

Tiyeni tiŵerenge Yesaya 10:5-6

5-Ambuye anati, "Tsoka kwa Asiliya. Ndodo ya ukali kwanga, m'dzanja mwache muli ndodo ya ukali wanga!
6-Ine ndidzaŵatumiza iwowo kukamenyana ndi mtundu wosandilemekeza (a Isirayeli), ndidzaŵalangiza anthu amene ali mu ukali wanga, kuti adzatenge zinthu ndikuziwononga, ndikuŵapondelera pasi ngati matope a mu njira."

-Mneneri wina wa Mulungu ankatchedwa kuti Yeremiya.
-Mneneri Yeremiya anapita ku mitundu iŵiri ya ku Yuda ija.
-Yeremiya anayiwuza mitundu iŵiri ya ku Yuda ija kuti ngati iwowo sakutsata njira ya Mulungu, Mulungu adzaŵatumiza a Babeloni kudzaŵagonjetsa iwowo pa nkhondo, ndikuŵachita ngati akapolo awo.

Tiyeni tiŵerenge Yeremiya 20:5

5-Ambuye anati, "Ndidzapereka kwa adani a (Yuda) chuma chonse cha mu mzinda muno, ndi zokolora zonse za ku minda, ndi zinthu zonse za mtengo wa pamwamba ndi zokulemeletsani zomwe za mafumu a ku Yuda. Adzazitenga ndikupita nazo ku Babeloni."

-Mulungu sanasinthe.
-Mulungu akufunabe kuti anthu onse asiye njira zawo ndikumatsata njira ya Mulungu.

-Mulungu adzapereka chilango cha imfa yosatha kwa anthu onse amene sakusiya njira za machimo ndikumatsata njira ya Mulungu.

ngati anthu aku Nineva.

-Mulungu akufuna kuti inu musiye kutsata njira ya machimo ndikumatsata njira ya Mulungu.

-Mulungu anasankhanso amuna ena kuti akhale atumiki ache kuti adziŵawuza anthu mawu ache.

-Amuna amene anasankhidwa ndi Mulungu kuti akhale atumiki ache ndikumaŵawuza anthu mawu ache ankatchedwa kuti Aneneri.

-Aneneri ena, Mulungu anaŵatumiza kwa anthu a mitundu 10 ya ku Isirayeli.

-Aneneri ena, Mulungu anaŵatumiza kwa anthu amitundu iŵiri ya ku Yuda.

-Aneneri ena, Mulungu anaŵatumiza kwa anthu a mitundu ina imene inkakhara pafupi ndi ku Isirayeli ndi ku Yuda.

-Aneneriŵa, ankaŵawuza anthu mawu a Mulungu.

-Aneneri ameneŵa, ankaŵawuza anthu kuti Mulungu akufuna kuti iwowo awononge milungu yawo yosema.

-Aneneri ameneŵa, ankaŵawuza anthu kuti Mulungu akufuna kuti iwowo asiye njira zawo za machimo ndipo adzitsata njira ya Mulungu.

-Mneneri m'modzi wa Mulungu ankatchedwa kuti Yesaya.

-Mneneri Yesaya anapita ku mitundu khumi ya ku Isirayeli ija.

-Yesaya anayiwuza mitundu khumi ya ku Isirayeli ija kuti



12. Kodi chinachitika ndi chiyani Solomoni atamwalira?
-Mitundu 12 ya a Isirayeli inagaŵikana ndikukhala mitundu iŵiri.
-Mitundu 10 ya ku mpoto, inakhala mtundu umodzi.

13. Kodi mitundu khumi  ya ku mpoto inkatchedwa kuti chiyani?
-Isirayeli.

14. Kodi mitundu iŵiri ya kumwera ija inkatchedwa kuti chiyani?
- Ayuda.

-Mulungu ankalankhula kwa anthu nthaŵi zonse kuti iwowo adzapulumutsidwa.

-Mulungu anaŵayitana amuna ena ndikuŵawuza kuti adzikaŵawuza anthu ena kuti iwowo adzapulumutsidwa.

-Mulungu anapereka mawu ache kwa Nowa, ndipo Nowa analankhula kwa anthu kuti iwowo adzapulumutsidwa.

-Mulungu anapereka mawu ache kwa Mose, ndipo Mose analankhula kwa Falawo ndi a Iguputo kuti iwowo adzapulumutsidwa.

-Mulungu anapereka mawu ache kwa Yoswa, ndipo Yoswa analankhula kwa a Isirayeli kuti iwowo adzapulumutsidwa.

-Tsiku lina Mulungu anamuyitana Yona amene anali m'modzi mwa a Isirayeli.

-Mulungu anamulamula Yona kuti atenge mawu ache ndikupita nawo kwa anthu oyipa amene ankakhala mu mzinda wa Nineva.

-Anthu amene ankakhala mu mzinda wa Nineva anali a Siliya.

Tiyeni tiŵerenge Yona 1:1-3a

1-Mawu a Mulungu anabwera kwa Yona, mwana wa Amitayi:
2-"Upite ku mzinda wawukuru wa Nineva ndipo ukalalikire motsutsana nawo, chifukwa chakuti kuyipa kwawo kwafika pa maso panga."
3-Koma Yona anati, "Ndikupita ku Tashishi."

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu ankafuna kuti Yona apite ku mzinda wa Nineva?

-Chifukwa chakuti Mulungu ankaŵakonda anthu a ku Nineva.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kuti aŵapulumutse anthu aku Nineva ku mphamvu ya sambi, imfa ndi Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Yona anathaŵa?
-Yona anathaŵa chifukwa chakuti iye sankafuna kuti apite ku mzinda wa Nineva.

-Kodi chifukwa chiyani Yona sankafuna kupita ku mzinda wa Nineva?
-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anali oyipa kwambiri.
-Chifukwa chakuti anthu a ku Nineva anali adani a a Isirayeli.
-Chifukwa chakuti Yona sankafuna kuti Mulungu aŵapulumutse anthu a ku Nineva.



Tiyeni tiŵerenge Yona 3:3-5 ndi 10

3-Yona anamvera mawu a Ambuye ndipo anapita ku Nineva. Tsopano Nineva unali mzinda ofunika kwambiri, oyenda masiku atatu.
4-Pa tsiku loyamba Yona anawuyamba ulendo opita mu mzindamo. Analalikira kuti, "Kwatsala masiku 40, Nineva adzayiwononga."
5-Anthu a ku Nineva anamukhulupilira Mulungu. Analamula za kusala kudya ndipo onse, kuyambira akulu akulu mpaka ana, anavala ziguduli.
10-Mulungu ataziwona zimene anachita iwowo ndi m'mene anatembenukira kuchokera ku njira zawo zoyipa, Iye anali ndi chisoni ndipo sanachite zowopsya zimene analankhula kuti adzazichita.

-Pa nthaŵi imeneyi, Yona anamumvera Mulungu ndipo anapita ku Nineva.

-Pa nthaŵi imeneyi, Yona anatenga mawu a Mulungu ndikupita nawo ku Nineva.

-Yona anaŵawuza anthu a ku Nineva kuti asiye njira zawo zoyipazo, ndipo atsate njira za Mulungu.

-Kodi anthu a ku Nineva anaŵamvera mawu a Mulungu amene Yona anaŵawuza iwowo?
-Inde.

-Mulungu akufuna kuti inu mukhale ngati anthu aku Nineva.

-Mulungu akufuna kuti inu mudzimvera ku mawu ache ngati anthu a ku Nineva.

-Mulungu akufuna kuti inu mudzikhulupilira mawu ache

10-Kenako Ambuye anayilamula msomba ija, ndipo inamulavulira pa mtunda.

-Kodi Mulungu anachita chiyani pamene Yona anavomereza kuti wamuchimwira Iye?
-Mulungu anayipangitsa msomba yayikuru ija kuti imulavulire pa mtunda.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupulumutsa Yona?
-Chifukwa chakuti Yona anavomereza kuti sanamumvere Mulungu.
-Chifukwa chakuti Yona anavomereza kuti anamuchimwira Mulungu.

-Kodi Mulungu anamuwuza Yona kuti asapite ku Nineva atatha kumupulumutsa?

Tiyeni tiŵerenge Yona 3:1-2

1-Kenako mawu a Ambuye anafikanso kachiŵiri kwa Yona:
2-"Upite ku mzinda wawukuru wa Nineva ndipo ukalalikire mawu amene ndakupatsa iwe."

-Mulungu sasintha.
-Mulungu sadzasintha.

-Mulungu ankafunabe kuti Yona apite ku Nineva.
-Mulungu ankafunabe kuti Yona atenge mawu ache ndipo apite nawo kwa anthu a ku Nineva.
-Mulungu ankafunabe kuŵapulumutsa anthu a ku Nineva.

-Kodi pa nthaŵi imeneyi, Yona anamumvera Mulungu ndikupita ku Nineva?



-Kodi Yona anatha kumuthaŵa Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Yona 1:3-10

3-Yona anapita ku Jopa, kumene anapeza chombo chili pa doko. Atatha kulipira ndalama, iye anakwera chombocho ndikupita ku Tashishi, kwathaŵa Ambuye.
4-Kenako Ambuye anatumiza mphepo ya mkuntho pa nyanja paja, ndipo mphepo ya mkunthoyo inayamba mwakuti chombocho chinatsala pang'ono kuti chisweke.
5-Anthu onse amene anali pa ulendowo anachita mantha ndipo aliyense analilira kwa Mulungu wache. Kenako anaponya katundu wawo mnyanjamo kuti chombocho chisalemedwe. Koma Yona anali atapita ku mbali yina ya chombocho kumene anagona tulo.
6-Kenako oyendetsa chombocho anapita kumene kunali Yona kuja ndipo anamufunsa kuti, "Kodi chifukwa chiyani ukugona? Dzuka ndipo umuyitane Mulungu wako! Mwina mwake Iye atikumbukira ife, ndipo sitiwonongeka."
7- Anthu amene anali pa ulendo wa pa nyanjawo, analankhurana wina ndi mzache kuti, "Tiyeni tiwombedze mawula kuti tiwone kuti zimenezi zikuchitika chifukwa cha ndani?" Atawombedza mawulawo, anamugwera Yona.
8-Chomcho anamufunsa Yona kuti, "Utiwuze ife, kodi zimenezi zikutichitikira chifukwa cha ndani? Kodi ntchito yako ndi yotani? Kodi ukuchokera kuti? Kodi kwanu ndikuti? Kodi mtundu wako ndi uti?"
9-Yona anayankha kuti, "Ine Mheberi, ndipo ndimapembedza Ambuye a kumwamba, amene analenga nyanja ndi mtunda."
10-Zimenezi zinaŵawopsya iwowo ndipo anamufunsa kuti, "Kodi chimene wapangachi ndi chiyani?" (Iwowo anadziŵa kuti iye ankaŵathaŵa Ambuye, chifukwa chakuti iye anali ataŵawuza kale iwowo.)

-Kodi Yona anatha kubisala pa maso pa Mulungu?

-Iyayi.

-Kodi Yona anatha kumuthaŵa Mulungu?
-Iyayi.

-Palibe amene angathe kumuthaŵa Mulungu.

-Ngakhale Satana ndi ziwanda zache sangathe kumuthaŵa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge Yona 1:11-15 ndi 17

11-Nyanja inayamba kuwopsya kwambiri. Chomcho anamufunsa Yona kuti, “Kodi tichite chiyani kwa iwe kuti nyanja ikhale bata kwa ife?”
12-Yona anayankha kuti, “Mundinyamule ine ndipo mundiponye mnyanja, ndipo nyanja ikhala bata. Ndikudziŵa kuti mphepo ya mkunthoyi yafika kwa inu chifukwa cha ine.”
13-Kenako amunawo anayesa kupalasa kuti abwelere ku mtunda. Koma analephera, chifukwa chakuti mphepo ya mkunthoyo inapyola poyamba paja.
14-Kenako analilira kwa Ambuye kuti, “Inu Ambuye, chonde musatileke ife kuti timwalire chifukwa chotenga moyo wa munthuyu. Musatiyimbe ife milandu yakupha munthu wosachimwayu, pakuti Inu mwachita m’mene mwafunira.
15-kenako anamutenga Yona ndikumuponya mnyanjamo, ndipo nyanjayo inachita bata.
17-Koma Ambuye anayiyitana msomba yayikulu kuti im’meze Yona. Ndipo Yona anakhala m’mimba mwa msombayo masiku atatu, usiku ndi usana.

-Kodi Mulungu anachita chiyani pa nthaŵi imene Yona sanamumvere Iye posapita ku Nineva?
-Mulungu anatumiza msomba yayikulu kukamumeza Yona.



-Yona anakhala m’mimba mwa somba kwa masiku atatu, usiku ndi usana.

-Kodi Yona anatha kudzipulumutsa yekha m’mimba mwa somba yayikulu ija?
-Iyayi.

-Kodi ndani amene anakatha kumupulumutsa Yona?
-Mulungu.

-Kodi anthu onse akufanana bwanji ngati Yona?
-Anthu onse sangathe kudzipulumutsa okha ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana ngati m’mene sanathere Yona kudzipulumutsa yekha m’mimba mwa somba ija.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kuŵapulumutsa anthu onse ngati m’mene anathera kumupulumutsa Yona.

-Kodi Yona anachita chiyani m’mimba mwa somba yayikulu ija?

Tiyeni tiŵerenge Yona 2:1

1-Kuchokera mkati mwa msombayo Ambuye anapemphera kwa Ambuye, Mulungu wache.
-Yona anavomereza kwa Mulungu kuti sanamumvere Iye.

-Yona anavomereza kwa Mulungu kuti anamuchimwira Iye.

-Yona anamuyitana Mulungu kuti amupulumutse iye.

-Kodi Mulungu anamupulumutsa Yona?

Tiyeni tiŵerenge Yona 2:10